

NYA_TTB_1067_SCRIPT

2 Petro : 2:10-19

Mutu : Chiphunzitso chonama chimadza ndi aphunzitsi onyenga

Landirani moni wa Kumwamba inu, wokonededwa anzanga apaulendo. Lero tiyamba ndi mau apa 1 Yohane 1:6, amene akuti, “Mulungu ndiye kuunika, ndipo mwa Iye mulibe mdima.”

Tsono mupologalamu yatha tinali kusanthula 2 Petro 2:5-9, pomwe timapitiliza kusanthula mutu wakuti chiphunzitso chonama chimadza ndi aphunzitsi onyenga. Ndipo lero pa 2 Petro 2:10-19, tipitiliza kuona mutu wakuti chiphunzitso chonama chimadza ndi aphunzitsi onyenga.

Pologalamu yatha tinatseka ndi mau akuti, Mulungu akusunga anthu ake pamodzi ndi woipa womwe monga mwanjira zake zomwe ifesitingazidziwe komanso sitingazimvetse. Mulungu akudziwa kusiyana pakati pa woipa ndi wolungama, inu ndi ine, sitingathe kusiyanyitsa. Tere, ndichifukwa chake adanena kuti zilekenizikulire pamodzi zidzaonekapokolola. Ndiye chomvetsa chisoni ndichakuti tirigu ndi namsongole zonse zikukulira pamodzi ndipo mau a

Mulungu akufalitsidwa m'nthawi yomwe ino.Koma patsiku lina, Mulungu adzazipatula zimenezi, pamene adzabwera kudzatenga ake kuchoka m'dziko lino pamene woipa adzatengedwa ku chionongeko chamuyaya.Kodi inu ndinu yani; namsongole kapena tirigu?

10.Koma makamaka iwoakutsatazathupi, m'chilakolako cha zodetsa kanthu, otsata chifuniro cha iwo eni, santhunthumira kuchitira mwano akulu.

Pano ndifuna kuyamba ndi mau akuti monga Mtumwi Petro afuna kutichenjeza ndi kutipatsa zida zodzitetzerakwa iwo afuna kutigwetsa, tsopano wafika ndime yotchula makhalidwe awo ndi kuwayenereza kuti Mulungu wolungama akhoza kuwasungadi ndi cholinga chowapatsa chilango choopsa choposa china chilichonse. Awa, ndiwo anthu amene achita choipa chomwe ndichonyasa kwambiri amene anafika podzitsitsa kapena kudzinnyazitsa kwambiri kuposa nyama yomwe ilibe nzeru.Tikunena za aphunzitsi onyenga pamodzi ndi anthu amene achita tchimo la chigololo koposa malire, nayambakugonana ndi amuna kapena akazi wokhawokha. Mtumwi Petro akunena kuti awa, monga momwe

anasungidwirakapena kutetezedweraKaini kuti adzakumane ndi kubwezerakwa Yehova. Ndipo Yuda 1:7-8, akufotokonzanso nkhani yomweyo pamene akupereka chitsanzo cha Sodomo ndi Gomora.Tamvani akunena kuti, “Monga Sodomo ndi Gomora ndi midziyakuzungulira, potsatana nayo, idadziperekakudama, ndi kutsata zilakolako zachilendo, iikidwa chitsanzo pakuchitidwa chilango cha moto wosatha.Momwemonso iwo m’kulota kwawo adetsamatupi awo, napeputsa ufumu, nachitira mwano maulemerero.”Kutanthauza kuti anthu awa, sakuchita uchimo wokha, komanso akunyoza malamulo achilengedwe ndi kunyazitsa chilengedwe cha munthu.Uku, ndiko kuchitira mwano ulamuliro wauzimu, umene unaperekedwa ndi kukhazikitsidwa ndi Mulungu kuchokera Kumwamba.M’chitidwe uwu, ndiwo umene ukhala pakati pa anthu amene apembedza mafano, opanda chikhulupiriro mwa Mulungu, m’ malo momwe muli uchimo ndi zonyenga zosaneneka. Awa, ndiwo angelo ndi anthu amene sakondwera ndi momwe Mulungu akuyendetsera dziko lake. Iwowa, sakondwera ndi ulamuliro wam’ mabanja, mumpingo ndi dziko lawo.Mwam’chitidwe uwu, awa ndiwo anthu amene akuuza Mulungukuti aone chinthu chilichonse panso pano kuti

ndichonyasa, popeza alibe kusiyanitsapazinthu zomwe zimapanga ufulu woona kapena weniweni. Mwanjira ina anthu amenewa amafunitsitsa kuchita chotheka kuti malamulo onse oletsachikhalidwe choipa chonse kuti achotsedwe ndi cholinga chakuti akwaniritsezolinga zawo pakukhazikitsa ufumu wawo m'mitima mwa anthu onse.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone nkondo zonsezi zikuchitika ndi ulamuliro wasatana kuti cholinga chake ndicho kuchotsa ulamuliro wa Mulungu kuti akhoze kukhala musamangika konse, nachita zawozonse monga afuna. Kodi inu, simudafikeapa?

Mtumwi Petro akunenanso kuti anthu wosalemekeza ulamuliro wa Mulungu, ndiwo anthu amene saona kapena kuopa ulemu ndi udindo wa munthu waulamulirowo. Mwanjira ina awa ndi anthu amene saopa malamulo a Boma komanso achipembedzo. Koma ndifuna kuti muone zimene adanena Paulo atazindikira kuti sanalankhule bwino pamaso pa akuru aulamuliro pa Machitidwe 23:4-5, pamene adamufunsa kuti, “Ulalatira kodi mkuluwa ansembe wa Mulungu? Ndipo Paulo anapepesa nati,

“Sindinadziwa, abale, kuti ndiye mkuluwa ansembe; pakuti kwalembedwa, usamnenera choipa mkulu wa anthu ako.” Kutsimikiza kuti mumtima mwa anthu otere muli chinthu choipa ndithu chomwe chimadana ndi ulamuliro ndipo amachita chotheke kutaya malamulo amene aletsa kuchita monga iwo afuna. Pachifukwa chimene anthu awa, ndiwo amene amalankhula mau owawa ndi onyozaanthu amene ali ndi udindo wokwaniritsamalamulowo.

11. Popeza angelo, angakhale awaposapolimbitsa mphamvu, sawaneneza kwa Ambuye mlandu wakuchita mwano.

Ndime ino ikunena kuti aphunzitsi achinyengowaamadzikweza chifukwa amachita zinthu zomweangelosangayerekeze kuchita. Pamene tiwerenga Yuda 9, tipeza mau akuti, “Koma Mikayeli mkuluwa angelo, pakuchita makani ndi mdierekezi anatsutsana za thupi la Mose, sanalimbika mtima kumchulira chifukwa chomchitira mwano, koma anati, Ambuye akudzudzule.” Nkhani pano ikunena kuti Mikayeli m’ngelowamkuluanalimbana ndi m’dierekezi pankhani yakuti thupi la Mose, lisakalowe m’dziko la malonjezano. Ndiye Mikayeli sanalimbane ndi m’dierekeziyo, koma

anangoperekaichi, m'manja a Yehova. Kunena kuti angeloamangopereka zolakwa za zolengedwa zinanzo kwa Ambuye, pokhala ndiye woweruza wolungama, komansowobwezera.Tere, uwu ndiwo mtima wodzichepetsa, womwe umasoweka pakati pa wokhulupirira.Tere, nkhani ikunena kuti angelo abwino amatipambanam'chibadwidwe ndi m'makhalidwe, m'mphamvu, mkuzindikira ndi m'chilungamo chonse. Ndiye tikuti angeloabwinowa ndiwo amene samakondwera ndi zochita zonyasa za zolengedwa zina. Mwa ichi, tikunena kuti anthu amene ali ndi kuthekerakokhala pamaso pa Mulungu, ayenera kukhala ndi mtima womvera chisoni onse amene anyazitsa dzina la Yehova. Tikunena kuti angelo awa samamemezaanzawo mwanjira ya miseche za angelo ena ayi. Ndiye nkhani ikuti inu ndi ine, tiyenera kutsazaangelo pamene tidandaula za woyipa kuti mowamvera chisoni ndi mopanda mkwiyo, tiyenera kuwapereka kwa Ambuye. Pofuna kutsimikiza kuti inu ndi ine, ndife ake akristu, amene ali wofatsa ndi wodzala ndi chifundo.

12.Koma awo, ngati zamoyo zopanda nzeru, nyama zobadwa kuti zikodwe ndi kuonongedwa, akuchitira mwano pa zinthu osazidziwa, adzaonongekam'kuononga kwawo.

Ndiye monga Petro waonetsa kale kuti aphunzitsi wonyengawa, asiyana kutari ndi angelo, pano akuonetsanso kuti aphunzitsi amenewa ndiwo wotsika kwambiri koposa nyama monga buru ndi kavalo, nyama zomwe zilibe chidziwitso china chilichonse, kotero kuti ndiwo amene ali pamzere wa ku chionongeko.Kutanthauza kuti munthu wadzitsitsa yekha kufika pamlingo womwe munthuyo alibe ntchito komanso chiyembekezo.Petro akunena mau amenewa chifukwa aphunzitsi onyengawa, akungonena zoipa pachinthu chilichonse chomwe alibe nacho chidziwitso china chilichonse.Lero lino, ndimomwe ziri kuno kwathu, kuti alipo anthu ambiri, amene alibe chidziwitso cha mau a Mulungu, koma ndiwo amene amakonda kunyoza mau a Mulungu.Ndiye tikunena kuti kalenso analipo anthu ena anzeru zawo za kusukulu, koma samadziwa mau a Mulungu. Mukumbukira a William Wilbefore, anali mkulu wotchuka amene anali phunguwa kunyumba ya malamulo ya a British. Iyeyu, anali kuledzera kwambiri, koma anatembenuka

mtima mofulumira, kotero kuti tsiku lina anamutenga bwezi lake, Edmund Burke, kuti akanve Uthenga Wabwino umene Mlaliki wina wotchuka, anali kufalitsa. Koma pamene a Edmund Burke anatha kumvera Uthenga uja, ananena kuti sanamvepo kanthu. Momwemonso alipo anthu ena amene ndi achipembedzo ndithu, kotero kuti amakhala m'chipembedzo kungothawazonyasakapena m'nyozowa m'dziko, koma osathawa chodetsa ayi. Tikunena kuti alipo anthu ena amangothawa kuchita zonyasa monga kuledzera, kuba, kuchita miseche ngakhale chiwerewereetc, pamene ali wosatembenuka mtima. Iwo amaganiza kuti ndicho chikristu, pamene siziritero.Awa, ndiwo anthu amene amaoneka achipembedzo kunjaku, pamene mkati mwawo alibe chiyanjano china chilichonse ndi Ambuye. Munthu uyu, ndiye amene ali woipa mumtima mwake, koma palibe chimene amalozapabvutolakelo. Awa, ndiwo anthu amene Petro akunena kuti “adzaonongekam’kuononga kwawo.”

13.Ochitidwa zoipa kulipirakwachosalungama; anthu akuyeserachowakondweretsakudyerera usana; ndiwo

mawanga ndi zirema, akudyereram'madyereroachikondi awo pamene akudya nanu.

Mtumwi Petro akunenetsa kuti anthu onse oipa kuphatikizapo aphunzitsi onyenga, adzalandira mphotho yoyenerana ndi uchimo wawo m'dziko limkudza m'tsogolo. Kutanthauza kuti anthu oterewa mwina samalandira chilango choyenera pansi pano, koma Kumwamba palibe kuzemba kapena kuthawa, aliyense adzalandira chilungamo. Kunena kuti mphotho kapena chilango cha munthu aliyense chiyenera kugwirizana ndi uchimo wake.

Ndiye Petro akunenetsa kuti alipo anthu ena amachita kuchita uchimo usana monyadiranamanena kuti uwu, ndimoyo wawo kotero kuti sipayenera kukhala wina kukhudzidwa pankhani yamoyo wawo. Pano ndifuna kupereka chitsanzo cha anthu a maudindo oimira gulu monga phungu kapena nduna. Ena mwa anthu amenewa amachita zinthu zonyasa kwambiri, namanena kuti zomwe akuchitazo ndi moyo wa iwo wokha suyenerakukhudza gulu la anthu, kuyiwala kuti zinthu zonyasa zomwe akuchitazozikuchititsa manyazi anthu omwe akuwaimira kunyumba ya malamulo. Anthu awa, ndiwo amene Petro

akuwacha kuti ndiwo mawanga kapena zirema m'dziko, m'mudzi kapena m'dera lomwe akuchokera. Mwanjira ina munthu wotere amaoneka kuti ndiye chodetsa kapena thope pa nsaru yoyera. Kutsimikiza kuti moyo wamunthu m'modzi ukhoza kunyazitsa kapena kudetsa mbiri ya dziko, dera kapena mudzi wake.

Ndiye zimachititsa manyazi chifukwa anthu otere, sakumva maganizo ya anthu ena, kotero kuti amadzisangalatsaokhapakukakamira ndi kukondwera ndi maganizo a iwo wokha amene ndi woipa kwambiri. Mwanjira ina, tikunena kuti anthu wotere, alibe kutsutsika kotero kuti amalimbikamum'chitidwe wawo ndipo amaona kuti masiku oipa ali kutali kapena kuti kulibe chilango china chilichonse. Ndipo anthu ena woterewaamakakamira kukhala pachipembedzonamadziyeretsa wokha mopanda ndi manyazi omwe.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kunenetsa kuti ngakhale anthu wotere amadzilimbikitsa kuchita zonyasazo ndi mau akuti ndimoyowa iwo wokha suyenerakukhudza ena, koma tikunena kuti uwu, simoyo wa iwo wokha popeza iye amayimira anthu ochuluka m'Boma komanso m'dziko. Kutanthauza kuti ngati anthu

amenewasangasiye m'chitidwe umenewu, ayenera kuchoka pamandopo ngati afuna kuchita monga moyo wawo ufuna, chifukwa amatinyazitsa. Kutsindika kunena kuti udindo uliwonse woimira anthu ena, uyenera kukhala ndi munthu amene ndiwoyenera, wamakhalidweosachititsa manyazi ndi wokhulupirika popeza Mulungu adaika ulamuliro pa iwowa. Zonsezi zimachitika chifukwa chakuti munthuyualipansipamphamvu ya uchimo, sakhoza kuona bvumbulutso la Mulungu popeza sangathe kuganiza bwino. Kodi atsogoleri athuwa ali ndi zowayenereza zimenezi?

14. Okhala nawo maso odzala ndi chigololo, osakhoza kuleka uchimo, kunyengereraiwo a moyo wosakhazikika; okhala nawo mtima wozolowerakusirira ana a temberero.

Nkhani pano ikunena kuti popeza aphunzitsi onyengawa akuchita zinthu monga moyo wawo ukhumba popanda kutsutsika, ndiwo anthu amene maso awo ali wodzala ndi chigololo, osakhoza kuleka tchimo. Kutanthauza kuti mitima ya iwowa ndi yodzala ndi zonyasa kotero kuti maso awo amafunitsitsa kuona zokhutitsa mtima wawo. Anthu awa, amafunansokukopa ena kuti agwe mum'chitidwe

wawo ndipo anthu amene moyo wawo usanakhazikike m'chisomo cha Mulungu, amakopeka mofulumira popeza moyo wawo ukhumba chuma. Ichi, ndichifukwa chake Petro akunena kuti ndiwo ana atemberero popeza ndiwo ali kale pansi chilango cha Mulungu.

15. Posiya njira yolunjika, anasokera, atatsata njira ya Balamu mwana waBeori, amene anakonda mphotho ya chosalungama.

Pano ndifuna kuyamba ndi mau akuti chipembedzo choona ndiyo njira yoongoka ndi yoona ndipo pamene tinena kuti munthu walowa kuthengo ndiye kuti waturuka m'chipembedzo ndipo watsata njira ya Balamu mwana waBeori. Apa, tikunena kuti Balamu ndiye m'neneri amene anachoka pachipembedzochenicheni, choona, kotero kuti anali kutumikira chifukwa chofuna kupindula, kapena kupeza chuma. Nkhani ikunena kuti Balamu anali kuchita chipembedzo chifukwa cha chikondi chapa chuma. Kodi atumiki otere mulibe m'dziko lathuli? Ndiye Yuda 1:11, akuchenjeza kuti, "Tsoka kwa iwo! Pakuti

anayenda m'njira ya Kaini, ndipo anadzionongam'chisokero cha Balamu chifukwa cha kulipira, natayikam'chitsutsano cha Kore.”

16.Koma anadzudzulidwa pa kulakwa kwake mwini; buru wopanda mau, walankhula ndi mau a munthu analetsakuyaruka kwa mneneriyo.

Petro mundime ino akuonetsa kuti Mulungu anagwiritsa ntchito njira yodabwitsa yofuna kudzudzula Balamu. Iyi, ndinjira momwe buru analankhula chifukwa cha tchimo loopsa, lomwe Balamu anachita. Ili ndi tchimo lomwe ndi linanyazitsa udindo wake.Nkhani ikunena za mneneri Balamu amene anali kutumikira ndi cholinga chofuna kudzilemeretsa yekha.Ndiye Petro akunena kuti umu ndimomwe tingawadziwire aphunzitsi onyengawa. Koma iwo ayenera kudziwa kuti Mulungu adzalanga ndithu aphunzitsi onyengawa.

17.Iwo, ndiwo akasupeopanda madzi, nkhunguyokankhika ndi mkuntho; amene m'dima wakudabiiuwasungikira.

Nkhani iyi, ikundikumbutsa tsiku lina m'nyengo yamvula momwe tinaona mabingu, ziphaliwali ndi mitamboyakuda yomwe

inasonkhana ndipo tinali ndi chithunzi chakuti tsiku limenelo kukugwa mvula yoopsya. Koma chodabwitsa ndichakuti pamene mphepo inaomba, nthawi yosakhalitsakunayera kotero kuti kunalibenso mvula ndipo anthu ambiri anadabwa ndi chimenechi. Tere, Uthenga ukuti, lero lino anthu ambiri akuthamangira aphunzitsi onyenga amene akunga ngati mitambo ndi ziphaliwalindi mabingu amene sabweretsa mvula. Kutanthauza kuti aphunzitsi ambiri masiku anu, amapereka chithunzi chakunja ngati kuti ali ndi Uthenga wa Mulungu, pamene alibendipo akunga zitsime zopanda madzi. Nkhani ikuti, lero lino anthu ambiri ali ndi ludzu la mau a Mulungu chifukwa mauwo sakuperekedwa kwa iwo. Kodi inu ngati mtumiki wa Mulungu, anthu akhoza kukuchitirani umboni kuti mumapereka madzi amoyo?

18. Pakuti polankhula mau otukumukaopanda pake, anyengerera pa zilakolako za thupi, ndi zonyasa, iwo amene adayambakupulumukira a mayendedweolakwawo;

19. Ndi kuwalonjezeraiwo ufulu, pokhala iwo okha ali akapolo a chibvundi; pakuti iye amene munthu agonjedwa naye ameneyonso, adzakhala kapolo wake.

Mtumwi Petro akuonetsa zomwe aphunzitsi onyenga amachita. Iye akunena kuti anthu amenewa ali ndi lusololankhula, kotero kuti amalankhula mau okongola ndipo amamveka bwino, pamene m'mauwo mulibe chinthu chilichonse chothandiza. Kutsimikiza kuti chimangokhala chipembedzo chokha chomwe chimangosangalatsapoonna ndi pakumva basi. Mtumwi Petro akunenetsa kuti ngakhale chipembedzo chikhale chokongola motani, koma sichodalirika ayi.

Wokonedwa anzanga apaulendo, ndifuna titsirize ndi mauakuti aphunzitsi onyengawa amalengeza mamasulidwe kwa akapolo, pamene iwo ndiwo akapolo akatangale, achigololo ndi zonyasa zina zotere. Mwanjira inaamalengezandi kulonjeza mamasulidwe pamene iwo ali akapolo a m'chitidwe wonyasa. Kutsindika kunena kuti aphunzitsi onyenga amalonjeza mtendere ndi mamasulidwe pamene iwosaudziwa mtendere weni-weni. Kodi inu ngati mtumiki wa Mulungu, mumazindikira chomwe mumalalikira kwa ena?

Kwalerotilekeza pano, koma tinali kusanthula 2 Petro 2:10-19, pamene timapitiliza kuona mutu wakuti chiphunzitso chonama chimadza ndi aphunzitsi onyenga.

Ambuye akuthandizeni kuti akupatseni maso auzimu momwe
mungathe kuona chinyengo chomwe chili m'dziko lathuli
ndipoambuyeakudalitseni lero. Amen!